3. Mpanda

Mpanda omangidwa bwino komanso okonzedwa pafupipafupi ukhoza kuthandiza kwambiri kuti nyama zakutchire zisalowe.

4. Kutchinga kwina

Kudzala heji wamtundu ulionse ndi njira yotsika mtengo komanso yothandiza ku nyama za mtchire. Njira ina ndikuyika minga kuzungulira khola la n'gombe koma ndi njira yosakhalitsa.

5. Kutaya Zinyalala mwadongosolo

Kutaya zinyalala mwadongosolo komanso malo oyenera zimathandiza kupewa kukopa nyama zakutchire kuti zibwere komwe tikukhala. Onetsetsani kuti dzenje lanu la zinyalala ndilalitali kosachepera mita imodzi ndi theka komanso ndilozondoka moloza pansi kuti nyama zisalowe. Kuwaza phulusa tsiku lililonse kumachepetsa fungo ndipo zimathandiza kuchepetsa kukopa afisi.

6. Kutsata ulimi wabwino

Kugwidwa kwa nyama kungachepetsedwenso potsata ulimi wabwino monga:

- Ziweto kukhala ndi m'busa masana
- Kugoneka nyama mukhola lomwe nyama zakutchire sizingafikemo (Kutchinga ndi mpanda kapena kumanga khola pokweza.
- Chotsani zitsamba ndi zina zonse zopereka mdima pa khola la ziweto.

7. Njira zosapereka chiopsyezo ku afisi

Gwiritsani ntchito njira zothandiza kuti nyama zisayandikire khola lanu.

<u>Kugwiritsa ntchito phokoso:</u> Zida zotulutsa mau zimadzidzimutsa nyama zakutchire potulutsa phokoso lomwe izo sizimayembekezera. Zinthu monga kuimba n'goma, zitini kapena mitengo komanso kukuwa ndikuyimba malikhweru.

<u>Zooneka ndi maso:</u> Zinthu zowala ngati nsalu, pepala komanso moto zimathandiza kuthamangitsa afisi ngati mwawaona akubwera.

Ndife ndani?

Carnivore Research Malawi (CRM) ndi pulojekiti yomwe imadzipereka pakafukufuku ndi kuteteza nyama mu Afirika. Ogwira ntchito ake ndi akatswiri a zasayansi komanso ophunzitsa anthu kumudzi.

Timapanga chiyani?

CRM ili ndi cholinga choteteza nyama zakudya nyama zinzake m'Malawi monse ndi cholinga chosunga chilengedwe komanso kuchepetsa mkangano wa anthu ndi nyamazi.

Anthu athu amafufuza zakhalidwe ndi chilengedwe cha afisi, nkhandwe komanso nyama zina zodya nyama zinzake. Timaphunzitsanso zothandiza anthu kumvetsetsa nyamazi komanso kuthandiza kuthana ndi mavuto obwera chifukwa cha nyamazi.

Kuti mudziwe zambiri zokhadza afisi komanso CRM tsegulani:

<u>www.carnivoreresearchmalawi.org</u>

kodi muli ndi vuto ndi afisi kapena nyama zina tatchulazi?

IMBANI NAMBALA YATHU YACHITHANDZO 5152

CRM tsopano ili ndi nambala **YAULELE** yachithandizo – imbirani akatswiri athu kuti akupatseni malangizo kapena akupezeni kwanu.

Wildlife Assistance Helpline: 5152

KUKHALA NDI AFISI

Afisi ndi nyama zopatsa chidwi kwambiri ndipo zimachita zinthu zopindulira dera lomwe izo zikupezekako.

Pamene malo awo okhala achilengedwe akuwonongedwa ndi kugawidwa, zikupangitsa kuti afisi azikhala moyandikana ndi anthu.

Ngakhale pali mantha aakulu pa nkhani zokhudza afisi, ndi zotheka kukhala nawo mwamtendere ngati patatsatidwa ndondomeko zoyenera.

Conservation Research Africa

Carnivore Research Malawi

Ndi chifukwa chiyani tikuyenera kukhala ndi afisi?

Malawi ndi dziko limodzi lomwe liri ndi anthu ochuluka mu Africa ndipo potero nyama ngati afisi zomwe zinalandidwa malo awo achilengedwe zikupezekanso m'matauni.

Pakuti mbali ina ya afisi ndi kutoleza, nyamazi zimathandiza kutola zinyatsi mu misika, malo ophera nyama, m'miseu, malo otaya zinyalala komanso kutola nyama zodzifera zokha ngati agalu. Izi zikupangitsa malo athu kumakhala aukhondo.

Afisi a madontho amathandiza kubwezeretsa chonde munthaka. Iwo amadya zakudya zosiyanasiyana kuphatikizapo mafupa ndipo chimbudzi chawo ndi manyowa amphamvu omwe amathandiza kubwezeretsa chonde mthaka.

Iwo amadyanso nyama zomwe zimatisowetsa mtendere monga makoswe okulirapo komanso agalu ongoyendayenda omwe amasowetsa anthu matendere.

Mphekesera ndi zikhulupiriro za makolo zimafotokoza kuti afisi ali ndi mphamvu zamatsenga kapenanso kuti munthu amatha kudzuka fisi. Palibe nyama imene ili ndi mphamvu ya matsenga komanso munthu sangasanduke nyama. Izi zimadza chifukwa chosanzimvetsetsa nyamazi pakuti zimayenda usiku.

Afisi akhoza kukhala mwa mtendere ndi anthu pokhapokha titachotsa kusamvetsetsana komwe kulipo.

Zoyenera kuchita tikakumana ndi afisi

Yesetsani kupewa kukumana ndi nyama za kutchire popezeka malo owala, ochuluka anthu komanso a phokoso. Musayende nokha kukada.

Ngati mwakumana ndi fisi ndipo sakuonetsa chidwi mwa inu, musamulabadire ndipo pitilizani kuyenda koma pan'gonopan,gono. Mulambalaleni ndipo **MUSATHAMANGE**. Kuthamanga kumakupangitsani kuti afisi akuthamangitseni. Mwazani maso kuti muwone ngati pali afisi ena pafupi.

Ngati fisi waonetsa chidwi mwa inu, pangani zotsatirazi;

• Khalani odekha ndipo musaonetse mantha

• Imani, musanthawe. Ngati mulenje, fisi amathamangitsa chinthu chomwe chikuthawa.

• Musagone pansi – kutero kumachulukitsa chidwi mwa fisi

• Ngati mwananyamula chakudya, chitayeni pansi. Ndipo ngati fisiyo akulimbana ndichakudyacho inu suthanipo pan'gonopan'gono

• ngakhale afisi ali alenje abwino iwo amatolezanso. Choncho pewani kunyamula chakudya usiku.

• Onani ngati mwaima pafupi ndi nyansi kapena nyama yakufa. Fisi amakhala ali ndi chidwi ndi zimenezo osati inuyo. Sunthanipo pan'gonopan'gono koma maso anu ali pa fisiyo.

• .Ngati fisi waonetsa chidwi ndipo akukuyandikirani, mwadzidzi yendani mayadi angapo momutsatira iyeyo kuti mumudzidzimutse ndikuti akuoneni inu ngati choopsya. Zunguzani manja anu mwa mphamvu. Pangani phokoso lokwera monga kukuwa kapena kukalipa ndipo onekani oopsya. Ndi zimenezi fisi akhoza kuthawa

• Ngati sichoncho sinthani zochita, khalani bata kwaka nthawi ndikuyenda modzidzimutsa kapena kupanga phokoso.Ngati fisi wakalipa, ndichizindikiro chakuti sakukuopani. Zikatere musatekeseke kapena kuthawa komabe musamuyandikirenso.

• Ngati mwanyamula chikwama, chipukuseni pamwamba pa mutu wanu. Kunyamula tochi kapena wizulo ndizothandizanso – muunikeni fisiyo m'maso ndipo ngati akukuyandikirani, muponyereni chinachake.

• Musachokepo mpakana fisiyo atasuntha. Sunthani pan'gono pan'gono maso anu ali pa fisiyo.

• Ngati zafika povutitsitsa kuti fisiyo wakulumphirani – zomwe sizichitika chitika – Menyanani naye fisiyo. Mumenyeni mutu wake pogwiritsa ntchito mtengo kapena miyendo. **Koma musathawe.**

Kuteteza ziweto ku afisi

1. Anthu ayenera kukhala tcheru

Kupezeka kwa anthu kumalepheretsa afisi kugwira ziweto. Kukhala ndi abusa owona ziweto kumachepetsa vuto lakugwidwa kwa nyama kusiyana ndikongozisiya zokha.

2. Galu olondera

Agalu olondera ziweto akhozanso kulowa m'malo mwa abusa makamaka usiku pamene nyama zili mkhola. Iwo amaphunzitsidwa kuti awadziwitse anthu pamene afisi afika. Agaluwa amakulira pamodzi ndi ziweto kuyambira ali an'gono ndipo amapanga ubale.